

“Langizo la Zipembedzo Lokhudzana ndi Nkhanza kwa Amayi

“Sitingakhalenso chete chifukwa tikupemphedwa kulimbikitsa ulemu waumunthu kwa chilengedwe chonse”

Magulu achipembedzo Aчитapo Kanthu pa Nkhanza kwa Amayi

1. CHIYAMBI

Dera lathu lakumwera kwa Africa likulimbana ndi mliri wa nkhanza zapakati pa amuna ndi akazi. Zimachitikira mnyumba zathu, m'malo ophunzirira, m'magulu azipembedzo, malo ogwirira ntchito komanso m'malo aboma. Amayi ndi atsikana amanzunzidwa, ndipo masiku ano abambo ndi anyamatanso. Zibwenzi zapamtima zomwe nthawi zambiri timaziganizira kuti zimakhala zachikondi, kusamalana ndi chitetezo tsopano zasanduka njira yozunzira ndi kuopsyezana.¹ Zotsatira zankhazazi kwa iwo amene akumana nazo ndizochititsa mantha kwambiri. Ngati anthu achipembedzo, tatengapo mbali kuti tithane ndi nkhanzayi.

Tikuzindikira kuchuluka kwa nkhanza pakati pa akazi ndi amuna mdera lathu komwe mayi m'modzi mwa amayi atatu aliwonse amakhala atachitidwapo nkhanza zina pamoyo wake. Kukumana ndi nkhanza zamtundu umenewu pamoyo wamunthu wamkazi ndikosiyana kuyambira 86% ku Lesotho mpaka 24% ku Mauritius,² tikuzindikira zovuta zomwe ziwerengerozi zimabweretsa, makamaka popeza ziwerengerozi zikungotiuza pang'ono zavutoli, chifukwa nthawi zambiri zandewu sizinenedwa. Bungwe la UNPFA limavomereza kuti nkhanza pakati pa akazi ndi amuna “ndi imodzi mwazomwe zachitika ponseponse, zosaululidwa kwenikweni komanso nkhanza yolekereredwa kwambiri padziko lonse lapansi.”³ Nkhanza yokhudza akazi ndi amuna imatchedwanso “mliri wakachetechete”, osati chifukwa cha kusaulula kokha, komanso chifukwa chakachetechete watonsefe, ndikuwakhallitsa chete amene akumana ndi nkhanza pachikhalidwe ndi chipembedzo komanso pakupotoza malemba opatulika, kunyoza, kusala, komanso mchitidwe wokakamiza. Ngati magulu azipembedzo talela chikhalidwe chokhala chete komanso chinsinsi pazankhanza pakati pa akazi ndi amuna.

Tikuvomereza kuti sitinaonetse chidwi polimbana ndi mlirihu monga momwe timayenera. Takhala tikuchepetsa zosowa za amayi ndi kuzunzika kwawo.⁴ Chifukwa chotenga nkhanzi iliyonse yokhudzana ndi kugonana komanso nkhanza pakati pa akazi andi amuna ngati zolaula, tazamitsa mchitidwe



wokhala chete. Komabe tikukhulupirira kuti zida zimene tili nazo mu miyambo yachipembedzo chathu zatikhazika patsogolo kuponya nkondo yothetsa nkhanza za akazi ndi amuna. Ngati m'mene zaonedwera molondola, “Atsogoleri achipembedzo amasinthitsa gulu lonse lachipembedzo, choncho atha kusokoneza gulu lonse la amayi omwe akumanapo ndi nkhanzazi - komanso chikhalidwe chachikale chosapilirana chosalola kufanana pakati pa akazi ndi amuna.”⁵ Kuteloku tataya udindo wathu woti “Osavulaza” ndipo m'malo mwake takhumudwitsa onse amene amatidalira.

Ife ngati atsogoleri achipembedzo tikukhumudwa kuti, ngakhale ena tamvetsera kulira kwa omwe adachitidwapo nkhanza zapakati pa akazi ndi amuna ndipo ndipo takhala tikupereka malangizo ndi chithandizo, ena mwaife sitinaperekeko malo achitetezo omwe anthuwa amasowa. Ndiponso sitiwonekera kwenikweni kumalo olimbanira ndi vutoli monga chipembedzo chathu chimatipemphera. Tikuvomereza kuti pakulangiza azimayi kuti azikhale muubwenzi wankhanza, kulalikira uthenga womwe umalimbikitsa mchitidwe wankhazazi, tasiya udindo wathu wokhala atetezi mdera lathu. Ndizachisoni kuti tikuvomereza kuti ena mwa atsogoleri athu ndi ena osankhidwa apezeka kuti ndiwolakwa ndiponso amangidwa chifukwa chochita nkhanza imeneyi. Tilinso ndi mlandu wonyalanyaza kuona mchitidwe wopondereza ndi zikhalidwe zina zomwe

zimagwirizana ndi malemba azipembedzo zathu. Ndiye ngakhale talankhulapo zodzudzula umphawi, sitimvetsa kwenikweni m'mene umphawi wa amayi umaonjezera ziopsyeyo zaowo ndi kudiyeredwa masuku pamutu ndi nkhanza. Tagwirizana kuchitapo kanthu molimbika kuthetsa nkhanza zapakti pa akazi ndi amuna m'magulu ndi m'mabungwe athu, komanso m'midzi ndi m'madera athu. Timadzipereka kuti tikhale malo achitetezo ndi chichiritso kwa omwe adakumanapo ndi zimenezi kuti anthu ozunzidwapo ndi khanzayi apeze chilungamo.

2. KUMVETSA M'MENE NKHANZA PAKATI PA AKAZI NDI AMUNA ZIMACHITIKIRA

Zochita zathu kuthana ndi vuto la nkhanza pakati pa akazi ndi amuna zingalimbikitsidwe ngati titayesetsa kumvetsetsa zina mwazimene zimayambitsa nkhanzazi. Malembo athu opatulika akunena poyera kuti tiyenera kufunafuna nzeru (Baha'u'llah Kitab-i-Aqdas, pp 51-52; Hoseya 4: 6 ndi Quran 20: 114). Kumvetsa mokwanira chomwe chimadzetsa nkhanza pakati pa akazi ndi amuna kudzatithandiza kuti tikhazikitse njira zabwino zothetsera vutoli. Sitingapitilize kukhala chete, kapena kuganiza kuti nkhanzazi ndi 'nkhani yachweniweni.' Nthawi zambiri zimakhala kusankha pakati pa moyo ndi imfa; imakhala nkhani yachitetezo chaumunthu, ulemu, chikhulupiriro, ufulu wachibadwidwe ndipo ndizofunikira paulemelelo wa mayiko onse.

Nkhanza zapakati pa akazi ndi amuna, monga SADC, imafotokozera ndi zones simene zimachitika kwa amayi, abambo, anyamata ndi atsikana potengera kuti ndi mkazi kapena mwamuna zomwe zimapangitsa kapena zingapangitse kuvulala mthupi, pazogonana, m'maganizo, kapena pazachuma, komanzo chiopsyeyo kuti achite izi, kapena kukhazikitsa ulamuliro wokwima kapena kulanda anthu ufulu wawo wamseri kapena wapagulu panhtawi yamtendere kapena nthawi yankhondo ndi mikangano ina.⁶

Magwero ankhanza pakati pa akazi ndi amuna ndi ambiri. Ngakhale mwamuna payekha amayenera kuyankha pazomwe amachita, tikuzindikira kuti pali machitidwe ndi zinthu zina zomwe zimafunikira kuzilingalira. Ndiye kuti, nkhanzazi ndi:

.....zotsatira zakusafanana pakati pa amuna ndi akazi komanso tsankho ndipo zimachitika chifukwa cha kukumana kwa zinthu ngati zikhaliidwe, zachuma komanso ndale. Mwadala kapena zongochitika zokha, nkhanza kwa amayi zimalimbikitsa mphamvu ndi ulamuliro wa amuna ndipo zimalimbikitsidwa ndi chikhalidwe chokhala chete ndi kusavommereza za kuopsya kwa zotsatira za nkhanza kuthupi ndi m'maganizo⁷.

Tikuzindikira kuti anyamata ndi abambo amathanso kuchitiridwa nkhanza zimenezi. Timazindikiranso kuti kufala kwa nkhanzazi pakati pamitundu ya athu aku Africa ndi zotsatira nkhanza zachiatsumunda chomwe chinalanda anthu athu chikhalidwe chamakolo ndikuwononga chikhalidwe cha anthu ambiri, ndiponso mwadala kusaukitsa anthu ambiri chifukwa chakufuna kupindulira ufumu wachitsamunda. Ndi munthawi imeneyi pamene anthu asowa chizindikiro chawo pamene nkhanza imakhala njira yokhayo yosankha, ndipo imakhala ngati chizolowezi, osakhala zachilendo. Komanso ndinthawi imeneyi pamene omwe alandidwa mphamvu yochita kalikonse m'madera awo, mozindikira kapena mosazindikira amayesetsa kusonyeza udindo ndi mphamvu zawo m'njira iliyonse yomwe angathe. Choncho, timawona kuti nkhanza imabweretsa nkhanza, ndipo iwo omwe anakhaulitsidwa ndi nkhanza amachitanso nkhanza zomwe zinawononga umunthu wawo.



Komabe, ndi azimayi ndi atsikana omwe amachitilidwa nkhanza zamtundu uliwonse. Zimenezi ndichifukwa chakusiyana mphamvu pakati pa abambo ndi amayi pagulu. Chipembedzo, chikhalidwe kusiyanyitsa pakati pa akazi ndi amuna kumapangitsa kuti akazi akhale osatetezedwa kunkhanzazi.⁸ Malingaliro amene amalimbikitsidwa ndi chipembedzo komanso chikhalidwe zapangitsa kuti amuna ambiri aziwona nkhanza ngati njira yovomerezeka yofotokozera zomwe akufuna. Kuwonjezera apo, chikhalidwe chamakolo chimaloa anyamata ndi abambo kuyika zokonda zawo patsogolo pa umoyo ndi ubwino wa atsikana ndi amayi. Ndiye kuti, kusiyana kwamphamvu pakati pa abambo ndi amayi kulikonseko ndi komwe kumayambitsa nkhanzazi.⁹

Tikuvomereza kuti zolembe zathu zopatulika nthawi zambiri zakhala zikugwiritsidwa ntchito molimbikitsa machitidwe ankhanza ndi kuwononga chikhalidwe. Koma palinso njira yomwe imapezeka m'malembawa – njira ya Mulungu yemwe amayima pamodzi ndi osauka ndi osalidwa kutsutsana ndi olemera komanso amphamvu. Choncho, kunkhani yankhanza yapakati pa akazi ndi amuna, ife tiyenera kuvomereza kuti kugwiritsa ntchito malembo opatulika kufuna kunena kuti pali chilungamo kuti mwamuna akhale wamphamvu kwambiri kuyenera kutsutsidwa pobwezeretsa mbali zina za malemba athu opatulika zomwe zimatsutsana ndi nkhanza komanso kugwiritsa ntchito mphamvu molakwika komanso omwe amalankhula zamtendere, chilungamo ndi machiritso, ndi dziko komwe munthu aliyense ali ndi mlingo wofanana chifukwa tonse tinalengedwa m'chifanizo cha Mulungu.

Ngakhale maboma athu komanso mabungwe aboma achitapo zabwino zothana ndi nkhanza zapakati pa akazi ndi amuna, zambiri zikuyenera kuchitika. Tikupitiliza kuwona amuna ena akuchitabe zankhanza kwa azimayi popanda chilango. Tikupitilizabe kuyika m'manda atsikana ndi amayi omwe aphedwa ndi amuna oterewa. Ndi zachisoni, kuti nthawi zina tikupitilizabe kumabisa nkhanzi zankhanzazi mnyumba zathu, mzipembedzo ndi m'madera athu.

Ife ngati atsogoleri achipembedzo tikuvomereza kuti ndife okhudzidwa kwambiri pankhani yazaumoyo ndi zachitukuko ndikuti tingachitepo zinthu zopewetsa ndikuchepetsa nkhanzazi komanso chiopsyezo chokhudzana ndi HIV.

2.1. Kulimbisidwa Kuchitapo Kanthu: Zitsanzo za Zochitika Zachipembedzo Kuthana ndi Nkhanza Pakati pa Akazi ndi Amuna Mdera Lino

LACHINAYI MU CHAKUDA: KUKANIZA NDI KULIMBIKIRA

Ntchitoyi ndiyosavuta koma yozama. Valani zakuda Lachinayi. Valani pini kuti mulengeze kuti muli m'gulu ladziko lapansi lomwe likulimbana ndi machitidwe omalola kugwiririra ndi nkhanza. Onetsani ulemu wanu kwa akazi omwe amapirira akakumana ndi nkhanza komanso kusowa chilungamo. Limbikitsani ena kuti adzakhale nanu. Nthawi zambiri utoto wakuda umagwiritsidwa ntchito ndi maganizo oipa amtundu wa anthu. Muntchitoyi utoto wakuda ukugwiritsidwa ntchito kusonyeza kutstutsa komanso kupirira.¹⁰

Ngakhale pali zovuta zochokera m'mbuyomu, sitinaleke ntchito yathu yolimbana ndi vuto lankhanza pakati pa akazi ndi amuna. Enafe taye setsa kuti mawu athu amveke ndikukhala powonekera patsogolo. Mwachitsanzo, ena mwa magulu athu azipembedzo amatenga nawo mbali pa Masiku 16 olimbana ndi nkhanza zapakati pa amuna ndi akazi chaka chilichonse. Takhala tikufuna kuzamitsa nzeru zoti nkhanza pakati pa amuna ndi akazi zili pakati pachipembedzo ndi uzimu wathu. Chinanso, ntchito yazipembedzo ya Lachinayi mu Chakuda yolimbana ndi nkhanzazi yayamba kugwira msewu m'dera lathu. Imeneyi ndi ntchito ya bungwe lamatchalitchi a dziko lapansi (World Council of Churches) lomwe likufuna kulimbikitsa magulu achipembedzo kuti azindikire mwachangu kuthana ndi nkhanza zimenezi. Limbikitsa anthu achipembedzo kuti ayike patsogolo ntchito yolimbana ndi nkhanzazi mdera lawo.

Mdera lonseli, mwayambika mgwirizano wazipembedzo wolimbikitsa anyamata ndi abambo pantchito yothana ndi nkhanza zapakati pa akazi ndi kuonetsetsa kuti anyamata ndi abambo asanduke zida zothanirana ndi nkhanza pakati pa akazi ndi amuna. Chonco:



M'malo ambiri muli maudindo, machitidwe ndi malingaliri omwe amadziwika kuti ndi oyenera munthu wabambo ndipo amagwirizana ndi umuna zomwe zimalimbikitsa ulemu ndi ubale wofanana pakati pa amayi ndi abambo ndipo ndi omwe amaonetsa kuti ukazi ndi wosiyana komabe wolemekezekanso. Poyang'anitsitsa kufanana pakati pa amuna ndi akazi, kaonedwe ka umuna kachonchi kamatsutsana ndi kamvetsedwe kachilungamo ndi machitidwe amakolo akale. Zosintha kaonendwe kaumuna katsopanoka ziyenera kukhala zabwino kwa aliyense, chifukwa zimatsimikiza kufunika kwakufanana, ndiponso ulemu kwa anthu amitundu yonse.

M'malo ambiri timaona kuti muli maudindo, machitidwe ndi malingaliri omwe amadziwika kuti ndi oyenera amuna ndipo amagwirizana ndi zachimuna zomwe zimalimbikitsa ulemu ndi ubale wofanana pakati pa amayi ndi abambo ndipo ndi omwe umaonetsa kuti ukazi ndi wosiyana komabe wolemekezekanso. Poyang'anitsitsa kufanana pakati pa amuna ndi akazi, kaonedwe kaumuna kachonchi kamatsutsana ndi kamvetsedwe kachilungamo ndi machitidwe amakolo akale. Zosintha zakaonedwe kaumuna katsopano ziyenera kukhala zabwino kwa aliyense, zimatsimikiza kufunika kwakufanana, ndiponso ulemu kwa mitundu yonse.¹¹

Tikuzindikira udindo wathu monga aphunzitsi ndi ofalitsa zidziwitso zomwe zingandize kupewetsa nkhanza zapakati pa akazi ndi amuna. Ena mwa maseminare ndi masukulu ophunzitsira zauzimu panopa amaonetsetsa kuti ophunzira akuuzidwapo nkhanzi yankhanzazi pamaphunziro awo. Ife tikuvomereza kuti tikupemphedwa kuti tipezere amene anakumanapo ndi nkhanza zotere malo achitetezo, komanso

MPINGO WA ANGLICAN KUMWERA KWA AFRICA, DAYOSIZI YA NATAL UNENAPO ZANKHANZA PAKATI PA AMUNA NDI AKAZI

Dayozizi ya Anglican ya Natal yakhala zaka zopitilira sikisi ikuyesetsa kuthana ndi mavuto okhudzana ndi nkhanza pakati pa akazi ndi amuna kudzera muzokambirana ku Sinodi ndikukhazikitsa mabungwe mu Dayosizi. Nthawi yomweyo, Bishopo Wamkulu Thabo Makgoba, yemwe ndi wamkulu wa mpingo wa Anglican kumwera kwa Africa (ACSA) amapempha Mpingo kuti uleke kuphiphiritsa nkhanza yankhazazi ndipo kuti uthandize mwaubusa anthu okumanapo ndi nkhanza osati kuwasala.

Ndi koyambirira kwa 2017, bishopu watsopano atasankhidwa, pamene tinayamba kupita patsogolo mu Dayosizi ya Natal. Kwa nthawi yoyamba tinali ndi bishopu woika patsogolo ntchito yothana ndi kusiyana kwa amuna ndi akazi komanso nkhanza pakati pa akazi ndi amuna. Kuteroku, iye anakhazikitsa munthu wosakhala m'busa woyang'anira ntchito ya Akazi ndi Amuna komanso zankhanza yapakati pa akazi ndi amuna. Gulu la Ulaliki wa Akazi ndi Amuna lopangidwa ndi anthu khumi amphatso zawo linakhazikitsidwa. Bishopu Dino adalengeza pachiyambi kuti iye sanagwirepo ntchito yokhudza akazi ndi amuna koma anali wokonzeka kuphunzira, chifukwa amadziwa kuti Mulungu amamuyitana kuti atsogolere Dayosizi kuthana ndi nkhanza pakati pa akazi ndi amuna. Cholinga chatsopano cha Dayosizi chinali chabe "Anthu Achikondi", ndipo mawu oimira ntchito ya kungwelo anali "Kukhala Magulu Achikondi".

Ndondomeko yoyamba ya woyang'anira inali kuyitanitsa Mlembe Wamkulu komanso Bishopu Wotsogolera wa Mpingo kumwera kwa Africa kumsonkhano wofunikira kuti adzagawane

Ndondomeko yawo yothana ndi nkhanza pakati pa akazi ndi amuna. Izi zinathandiza Bishopo ndi omuthandiza kuti amvetsetse kufunika ndi mphamvu yogwiritsa ntchito udindo wawo potsogolera ntchito.

Ntchito yozindikiritsa inayambitsidwa kudzera mumisonkhano inayi ya Atsogolero azipembedzo imene a Bishopu adayitanitsa panthawi yokwana zaka ziwiri kuti athane ndi mavuto osiyanasiyana okhudzana ndi nkhanza za akazi ndi amuna. Panali ena onyinyirika, koma ambili amavomereza, popeza zimadziwika kuti nkhanza zankhazazi zimayenera kuwakhudza abusa. Misonkhanoyi idapangitsa kuti pakhale dongosolo la zokambiranazi m'madera, mzigawo ndi m'miphakati, ndipo atsogolero achipembedzo adayambitsa ndondomeko zantchito zachigawo m'maboma 11 (Ma Archdeacons) mu Dayosiziyo.

Komabe, woyang'anira anafotokozera Bishopu zankhawa yake pazopitiliza maphunziro pomwe amakhala chete pankhani yonena za nkhanza zomwe zimachitika pakati pa akazi ndi amuna mutchalitchi. Izi zimanenedwa potengera ziphunzitso ndi machitidwe amtchalitchi omwe amalolera kuti nkhanza zizichitika ndiponso mphekesera kumawanda kuti zimenezi zimachitidwa ndi atsogolero ena amatchalitchi. Anavomereza ndikudzipereka pantchito yolengeza poyera kuti Dayosizi inali ndi mfundo yosalekerera zachipongwe ndiponso kuti madandaulo aliwonse okhudzana zachipongwe zachiwerewere zochitidwa ndi atsogolero ena achipembedzo kapena atsogolero wamba adzathana nawo.

Ndiponso, Bishopo Dino adadabwitsa atsogolero achipembedzo omwe anali pamsonkhano wamgwirizano wa 'We Will Speak Out SA' kuti vuto lalikulu lokhudzana ndi nkhanza pakati pa amuna ndi akazi ndi chiphunzitso chosatsutsa lingaliro loti 'utsogolero

wamwamuna' komanso 'kugonjera kwamkazi'.

Izi zinalimbikitsa ena omwe ananzunzidwapo kuti abweretse milandu kwa aBishopu, ndipo zofufuza zinachitika motsatira Malamulo Aubusa ndi Malamulo a Dayosizi okhudzana ndi mchitidwe wogonana, ndipo milandu yofufuzidwayo inalandiridwa. Zofufuzazi zinawulula zolakwika zina m'malamulo ndi malangizo amachitidwe, zomwe zakonzedwa. China chimene chimasokonezetsa kuti milandu imvedwe ndi kuchititsa mantha kwa nkhanza, anthu amaopa kuchitira umboni, ndipo zimenezi zitha kubweretsa kugawikana mumphakati ndi kuwopsyezedwa kwa odandaula komanso mboni.

M'chaka chapitachi, Ofesi ya Bishopu Wamkulu yakhala ikuyang'ananso milandu ina, ndipo zotsatira zake ndi zosiyanasiyana. Bishopu wakhazikitsa bungwe lachitetezo mumpingo, 'Safe Church Commission,' yomwe ikupanga chikalata chachitetezo m'miphakati. Kutsatira zomwe taphunzira pa izi, Bungweli ndi mabungwe ena olilangiza analemba zikalata zofunikira ndi zamalamulo, zomwe zangovomerezedwa ndi Sinodi Yachigawo, yomwe ndiye bungwe lalikulu kwambiri lopanga malamulo mu ACSA.

Iyi ndiye nkhanza yakusinthana komanso nkhanza yokhudza kuwopsa kwa opulumuka komanso atsogolero achipembedzo akulu. Ndipo tikuyitanidwa kwa ife omwe tili mgulu la mabungwe azipembedzo kuti tikumbukire kufunikira kokhala olimba mtima mogwirizana komanso ndi atsogolero athu omwe ali okonzeka kuyika pachipembedzo kuyankha kuyitanira kwa Mulungu kuti azule zinsinsi zonse zobisika zomwe zimafooketsa kukhulupirika kwa mboni yathu komanso kudalirika kwa utumiki wathu ngati malo opembedzera ndi ochiritsira.

kuwonetsetsa kuti tikunena zowona zosapeputsa mavuto ofuna kuphukiranso pamoyo wawo kapena zomwe zingaikenso miyoyo yawo pachipembedzo. Tikuzindikira kuti kudzera m'malemba athu opatulika, miyambo, ziphunzitso ndi zikhulupiriro za zipembedzo za m'madera zingabweretse ulemu waumunthu, kulimbika kaganizidwe kabwino ndikupereka malangizo ndi ziphunzitso za kugonana zopangitsa kudzigomera pamoyo.

Pakati pathu, panopa tili ndi magulu azipembedzo amfundo zothanirana ndi nkhanza zapakati pa akazi ndi amuna, kuntchito komanso

m'magulu achipembedzo. Pogwira ntchito ndi anthu achidwi mdera lathu ndikupanga mgwirizano ndi anthu ena akufuna kwabwino, tawonetse kuti titha kuthana ndi nkhanza zachilungamo mwachidwi komanso mwachifundo.



Pang'onopang'ono koma molimba mtima tikutenga malo athu oyenera pomenyera ufulu wa chilungamo. Kupyolera mu mgwirizano, kugawana chuma ndikukambirana mosaopa, titha kuyamba kulingalira za dziko latsopano mdera lathu momwe simulowedwa nkhanza pakati pa akazi ndi amuna ndipo munthu aliyense akuphukira.

3. KULIMBITSA ZOCHITAPO ZATHU PANKHANZA ZAPAKATI PA AKAZI NDI AMUNA

Ngakhale tayamba kuchitapo kanthu pothana ndi nkhanza zapakati pa akazi andi amuna, tikuvomereza kuti padakali zambiri zoyenera kukonzanso. Njira zotsatirazi zingathandize kuthana ndi mliriwu.

3.1. Zamitsani ndi Kutchukitsa Chiganizo choti Anthu Onse ndi Olengedwa Zofanana

Malembo athu opatulika akunena poyera kuti anthu onse adalengedwa ofanana ndi ufulu wokhala ndi moyo wochuluka.

3.2. Limbanani ndi Mphamvu Mwanzeru ndi Kulimba Mtima

"Amene amaberekedwa kumsana kwamzake sazindikira kutalika kwamtunda wa kutauni"

(Mwambi wa ku Africa)

Nthawi zambiri, malingaliro amene amabweretsa nkhanza pakati pa akazi ndi amuna amathandizidwa kapena kuloledwa ndi kagwiritsidwe ntchito kolakwika kamalembo opatulika ndi miyambo yathu. Ziphunzitso zachipembedzo ndi zolumikizana

nazo zimapereka mpata wofunikira kuti anthu anene zomwe akumana nazo pankhazazi. Zimenezi zikhoza kuthandiza kapena kulepheretsa.

Tiyenera kukhala olimbika mtima kuti tionenso kamasuliridwe ka Malemba Oyera ndikulola zolemba zina kuti zitsutsane ndi m'mene tigwiritsira ntchito Malemba molakwika. Mwachitsanzo, ziphunzitso zomwe zimakhazikitsa ulamuliro wamwamuna popanda kuzindikira kufunika kwa kulemekezana, kukondana komanso kugonjera chifanizo cha Mulungu mwa munthu aliyense, zitha kubweretsa kugwiritsa ntchito mphamvu molakwika ndiponso zingagwiritsidwe ntchito yovomereza nkhanza pakati pa akazi ndi amuna. Iye ngati atsogoleri achipembedzo tilinso ndi mlandu wogwiritsa ntchito mphamvu zathu molakwika ndikuvomereza chikhaliidwe chokhala chete ndiponso kusalanga olakwa m'mipingo yathu zomwe chathandiza kukhazikitsa nkhanzazi. Tikudzipereka kuti tichotsa mchitidwe umenewu ngakhale utachitidwa ndi audindo athu, ndikuyika njira zoletseratu zonyansa zotsagwirizana ndi achilungamo cha Mulungu.

Tidzachita chotheka kulimbikitsa chilungamo pakati pa amuna ndi akazi mdera lathu kuti tithane ndi nkhanza zimenezi. Zolemba zathu zachipembedzo zimatilankhula zamtendere, chikondi ndikukhalira limodzi mogwirizana komanso kulemekezana.¹²

3.3. Limbikitsani Kuphunzitsana

Kugawana machitidwe abwino komanso kuphunzitsana pakati pathu ngati magulu azipembedzo kudzera pakusinthana zidziwitso ndi misonkhano pafupipafupi m'magulu onse azipembedzo zidzathandiza kuti zochita zathu zizikhala zoyenera. Iye ngati atsogoleri achipembedzo tikufuna kugwiritsa ntchito maudindo athu ngati atsogoleri ammadera kuti tithandize kukonza zokambirana zankhanza pa amayi.

Zitsanzo zamgwirizano wa mabungwe opangidwira makamaka



kuti atsegule mwayi wophunzitsana amapezeka mu miyambo yambiri yachipembedzo mizipembedzo zonse.¹³

Miyambo yathu yachipembedzo imatenga nzeru mchisamaliro ndi chilungamo. Izi zikutsimikizidwa ndi zolemba zathu zopatulika monga zanenedwera pansipa.

3.4. Limbikitsani Kukambirana ndi Mabungwe Othana ndi Nkhanza Zapakati Pa Akazi ndi Amuna

Ngakhale pali zisonyezo zamgwirizano ndi mabungwe komanso anthu ofuna akuthana ndi nkhanza pakati pa akazi ndi amuna kuposa gulu lachipembedzo, izi zikuyenera

Pamene malo athu ophunzitsira kuchitapo kanthu kwambiri

pazothana ndi nkhanza pakati pa akazi ndi amuna, tiwapemphe kuti ayike mtima pantchito ya kafukufuku ndi kulemba. Zimenezi zidzathandiza kuti kulowererapo kwathu kukhale kwaphindu chifukwa nzeru zake zidzachokera muzotsatira zakafukufuku. Kuwonjezera apo, tidzayesetsa kulemba zochita zathu pankhani ya nkhanza pakati pa akazi ndi amuna. Kulemba kwakhala chimodzi mwa mavuto athu aakulu. Monga tawonera, takhala tikugwiritsa ntchito mphamvu zambiri 'kuchita' m'malo molemba zantchito zathu ndi zomwe tikukumana nazo. Tikulonjeza kuti tithana nalo vuto limeneli pakulemba zimene timachita pothana ndi nkhanza yapakati pa akzia ndi amuna ndikuonetsetsa mwatcheru zomwe takumana nazo kuti tipititse ptsogolo machitidwe athu ndikuwonjezera mphamvu zathu zodzisinthira tokha, zipembedzo zathu, madera athu ndi malo achipembedzo, ndiponso miyoyo ya munthu aliyense.

3.5. Limbikitsani Kafukufuku ndi Kulemba za Machitidwe a Chipembedzo Pothana ndi Nkhanza Pakati pa Akazi ndi Amuna

Pamene malo athu ophunzitsira kuchitapo kanthu kwambiri pazothana ndi nkhanza pakati pa akazi ndi amuna, tiwapemphe kuti ayike mtima pantchito ya kafukufuku ndi kulemba. Zimenezi zidzathandiza kuti kulowererapo kwathu kukhale kwaphindu chifukwa nzeru zake zidzachokera muzotsatira zakafukufuku. Kuwonjezera apo, tidzayesetsa kulemba zochita zathu pankhani ya nkhanza pakati pa akazi ndi amuna. Kulemba kwakhala chimodzi mwa mavuto athu aakulu. Monga tawonera, takhala tikugwiritsa ntchito mphamvu zambiri 'kuchita' m'malo molemba zantchito zathu ndi zomwe tikukumana nazo. Tikulonjeza kuti tithana nalo vuto limeneli pakulemba zimene timachita pothana ndi nkhanza yapakati pa akzia ndi amuna ndikuonetsetsa mwatcheru zomwe takumana nazo kuti tipititse ptsogolo machitidwe athu ndikuwonjezera mphamvu zathu zodzisinthira tokha, zipembedzo zathu, madera athu ndi malo achipembedzo, ndiponso miyoyo ya munthu aliyense.

ZOWERENGA

1. Gender Links, "Chapter 5: Gender-Based Violence," SADC Gender Protocol 2018, 153. <https://genderlinks.org.za/wp-content/uploads/2018/08/Chap5-Baro-2018-GBVfin.pdf>
2. Gender Links, SADC Gender Barometer 2009. https://www.sadc.int/files/5013/5435/5210/SADCGenderBarometer_2009.pdf
3. UNFPA Engagement in ending Gender-based Violence: Advocacy and Policy Capacity Development Knowledge Management Service Delivery: Results of a mapping exercise. 2016. Available at https://www.unfpa.org/sites/default/files/resource-pdf/UNFPA_Brochures_on_GBV_Prevention_and_response.pdf
4. See for example, D. B. Gennrich, 'Liturgy, Faith and Sexual and Reproductive Health Rights: A Study of Liturgical Reframing in the Anglican Church of Southern Africa,' A thesis submitted in fulfilment of the degree of Master of Arts in the School of Religion, Philosophy and Classics in the College of Humanities, University of KwaZulu-Natal, Pietermaritzburg, 2017, 18.
5. E. le Roux, 2015 A scoping study on the role of faith communities and organisations in prevention and response to sexual and gender-based violence: Implications for policy and practice, 48. Available at: https://jiflc.com/wp-content/uploads/2015/10/Le-Roux_SGBVFaith-scoping-study_REPORT_30Sept15.pdf
6. <https://www.sadc.int/issues/gender/gender-based-violence/>
7. UNFPA Asia and the Pacific Regional Office, "Preface," in A Mapping of Faith-based Responses to Violence against Women and Girls in the Asia-Pacific Region. Bangkok, 2012, 7.
8. See, for example, T. S. Maluleke and S. Nadar, "Breaking the Covenant of Violence against Women," Journal of Theology for Southern Africa 114, 5-17.
9. For a detailed discussion of the causes of gender-based violence, as well as global and regional efforts to address it, see the SADC Regional Strategy and Framework of Action for Addressing Gender Based Violence 2018 – 2030. Available at: https://www.unodc.org/documents/southernafrica/Stories/2019/SADC_Regional_Strategy_and_Framework_for_Action_on_GBV_-_FINAL_September_2018_-_ENGLISH_VERSION.pdf
10. <https://www.oikoumene.org/en/get-involved/thursdays-in-black>. Badges and faith based resources to take this campaign forward are available at <https://www.thursdaysinblack.co.za/>
11. UN Women Training Centre, Self-Learning Booklet: Understanding Masculinities and Violence Against Women and Girls. San Domingo, UN Women Training Centre, n.d., 15.
12. Fortune, M. (1987). Keeping the faith: Guidance for Christian women facing abuse. San Francisco: Harper.
13. Faith to Action Network, ACT Ubumbano, We Will Speak Out, and Side by Side are a few examples.
14. S. Parry, Responses of Faith-Based Organisations to HIV/AIDS in Sub-Saharan Africa. Geneva: World Council of Churches, 2003, 17.

Mtsiriziro

Ife, ngati atsogoleri achipembedzo komanso anthu achiyembekezo, tikudzipereka kuthetseratu nkhanza pakari pa akazi ndi amuna. Timakhulupirira kupatulika kwa moyo komanso kuti thupi la munthu ndiloyeretsedwa. Choncho, ndiloyenera kutetezedwa osati kuvulazidwa. Liwu lathu ngati anthu achipembedzo ndilofunika kwambiri kuti tipeze njira zothetsera nkhanza zapakati pa akazi ndi amuna. Kukhala chete ndi kumakhala 'amantha' pankhani zokhudzana ndi nkhanzazi sichinthu chololedwanso. Ndiudindo wathu kuyika mtima pazofuna zathu kuti derali likhale losandulika, laphindu, lanyonga, komanso lopanda nkhanza pakati pa akazi ndi amuna, pogwiritsa ntchito mipata yonse yomwe tili nayo kulankhula ndikulimbikitsa zochita polimbana ndi mliriwu. Ngati asungi amalembo opatulika athu, tikudzipereka kulimbikitsa ntchito yowunika malembo achipembedzo ndi kuyang'ana njira zamakono zotanthauzira momasuka zomwe zingalimbikitse umoyo ndi ubwino wa anthu onse, kuphatikizirapo anthu omwe anakhaulapo ndi nkhanzazi.

Tidzayesetsanso kukhazikitsa, mopanda kubisa, mfundo zomwe tili nazo kale; kusintha zomwe ndizofunika kukonzedwa; ndikulemba mfundo zatsopano pomwe pakufunika kutero. Tikuyimira limodzi ngati atsogoleri achipembedzo, ngati othandiza omwe anakhaulapo, olankhulapo pamchitidwe wosalanga olakwa komanso kusolidwa ndi kunyozedwa kwa amene ananzunzidwapo. Pamodzi, tidzalimbana ndi zipembedzo ndi zikholidwe zopondereza akazi komanso miyambo yathu kuti tithane ndi zovuta zilizonse zokhudzana ndi kusowa kwa chilungamo, ndipo tidzakhalala okonzeka kuyankha mafunso tikadzafunsidwa.

Tikupita ndi cholinga ca chiyembekezo ndiponso pempho lochitapo kanthu.

MALANGIZOWA ANAKONZEDWA NDI MABUGWE AWA



ACT UBUMBANO



The Methodist Church of Southern Africa
A Christ healed Africa for the healing of nations

actalliance

